NDONDOMEKO YOSAMALIRA BULOKO YA NYANJA
GULUPU NYANJA
MFUMU YAYIKULU NTHONDO

NTCHISI DISTRICT ASSEMBLY

YOKONZEDWA NDI ANTHU AKWA NYANJA MOTHANDIZANA NDI ALANGIZI AZA NNKHALANGO

NDI THANDIZO LOCHOKELA KU IFMSLP

MUNTHU WOLUMIKIZANA NAYE
GERLAD PHIRI (Phone : 09013284)
KANKOWE II VILLAGE
G.V.H. NYANJA
TA NTHONDO
NTCHISI

JUNE, 2008

ZAMKATI **Tsamba**

Mau oyamba	1
Kufotokoza za mmene Buloko ya Nyanja ilili	1
Udindo wosamalila Nkhalango	1
Malile ya buloko	1
Umwini wa nkhalango	1
Anthu ogwilitsa ntchito	1
Ntchito za Nkhalango	2
Mapo ya Nkhalango ya ntchisi kuonetsa Buloko ya Nyanja	3
Zigawo za kasamalidwe ka Nkhalangoyi	4
Mapu ya Buloko ndi zigawo zake	4
Cholinga chachikulu cha ndondomekoyi	5
Zolinga zing`ono zing`ono	5
Malamulo ya kagwilitsidwe ntchito	5-6
Dongosolo la kagwilitsidwe ntchito	6-7
Chigawo chachitatu (FMU 3)	8
Chigawo chachiwili (FMU 2)	8
Chigawo chachiwili	9
Chotengedwa ku nkhalango Mankhwala (FMU 3)	10
Chotengedwa ku nkhalango zipatso (FMU3)	11
Chotegedwa ku nkhalango Luzi (FMU 3)	12-13
Ndondomeko ya kagwilidwe ka ntchito	13-15
Ndondomeko yoyendela nkhalango	15-17
Dongosolo lochitila kalondolondo	17-18
Dongosolo la zachuma	18-19
Malamulo oyendetsela buloko ya Nyanja	19-26

KUTHOKOZA

Tiri okondwa pofuna kuthokoza anthu osiyanasiyana amene apangisa kuti ndomeko yosamalira Buloko ya Nyanja ipangidwe motere: Agulupu a Nyanja, T/A Nthondo, Agulupu Anguluwe pamodzi ndi mafumu ndi anthu onse. Chithokozo chipitenso kwa bambo S.C. Goneta, G.K. Chinaya, Y. Mndefu chifukwa cha upangiri wao ndiponso bamboo P. Muhosha ndi bamboo F.J.L. Maluwaya chifukwa cha mathandizo onsiyanasiyana.

Tikuthokozanso aku Regional Forestry Office (PCU) monga Bambo Ketulo, Mai Gama, Bambo C. Buss chifukwa cholumikiza ntchito yonse komanso sitikuyiwala kuthokoza EU (IFMSLP) chifukwa cha thandizo la ndalama zogwirira ntchitoyi.

MAU OYAMBA

Ndondomekoyi yapangidwa pochita kafukufuku wa mnkhalango komanso kukambilana pakati pa anthu ozogulira a gulupu a Nyanja, alangizi a zankhalango, mafumu, ma Gulupu ena ndi Gogo Chalo Nthondo.

Cholinga cha ndondomekoyi ndichofuna kuwapatsa mphamvu anthu amwa Gulupu Nyanja kuti athe kusamalira kuno Buloko ya Nyanja pamodzi ndi unduna wa zankhalango ndi kugwiritsa bwino antchito zinthu zopezeka mnenemo motsatira malimulo azankhalango amchaka cha 1996.

Anthu onse wogwiritsa ntchito zinthu zankhalango mdelali ayivomereza ndondomekoyi. Zimene zayikidwa ndondomekoyi ndi monga: Kasamalidwe ndi kagwiritsidwe ntchito kazinthu zopezeka mu Buloko koma mitengo yazinthu yopezeka menemo kagawanidwe kaphindu komanso kagwiritsidwe ntchito ka ndalama zopezeka pogulitsa zinthu zopezeka mu Buloko

UDINDO WOSAMALIRA NKHALANGO

Ndondomekoyi idzalongosoledwa ndi bungwe la za nkhalango la Nyanja Buloko pamodzi ndi alangizi aza nkhalango. Bungweli ndilodziwika bwino, lili mwa a Gulupu a Nyanja, gogo chalo Nthondo ndipo lili mukawundula ku ofesi ya za nkhalango ya Ntchisi.

KUFOTOKOZA ZA MMENE BULOKO YA NYANJA ILILI

Bulokoyi ili mkati mwa nkhalango ya boma ya Ntchisi ndipo ili kufupi ndi midzi yozungulira Gulupu Nyanja monga Kankowe I ndi II , Zamnyunda, Zambala I ndi II, Ngoma, Nyanja I ndi II, Nkhalawangwe. Bulokoyi yayandikana ndi buloko ya Mandwe cha ku mpoto ndi buloko ya Chifwerekete cha ku mwera. Kuchokera ku Ntchisi boma pali ntunda wokwana 13.5km kupita cha kumvuma. Mnkhalangoyi muli mitsinje imene ili ndi madzi wosaphwa monga: Dwazi, Kampongozi, Chimasomaso, Nachiwaliza, Navipwete, Nachiwale ndipo anthu ozungulila timapindula nayo mitsinjeyi pochapamo zovala, kuwedzamo nsomba. Dothi lopezeka mu bulokoyi ndi la chifulankhululu lophatikizana ndi mchenga. Nkhalangoyi ndi ya mtundu wa sanga kutanthauza kuti mitengo imene ikupezeka mkatimo yambili ndiya sanga. Mitengo yina imene ikupezeka ndiya msenga, msuku, kadale, katope, mbawa, nkulasinga, ntukumphako, ntanthamphete, Mbwabwa, nkulo, kasokolowe, mbanga, chiyere, kanung'unung'u, nkuyu, msolo, mphsyiphsya,Mbura, mkalakati, Thombozi, kamphoni, mpasa, manjaatali. Nkhalangoyi ndi yayikulu pafupifupi 707.5ha ndipo ndiyovalila bwino mbali zambili kupatula malo ena ndi ena okwana pafupifupi 11ha omwe kwakhala kukugwa zakudya zotchedwa matondo. Mbali imeneyi anthu akhala akudula mitengo ndicholinga chofuna kutola tizilombo timeneti. Anthu amene akhala akutiwonongela mitengoyi ambili ndi wochoka madera ena monga kuvikula, kayoyo, chikhwakhwa, ndi madera ena akutali ngakhale ku Ntchisi Boma. Mnkhalangomu muli mitengo ya masaizi yosiyanasiyana kuyambila mikangala, nsichi, phaso, mitanda, nkhuni ngakhalenso matabwa.

MALIRE YA NKHALANGO

Malire ya buloko yathu ndiyodziwika bwino chifukwa malo ena yatsata mitsinje mbali zina kumene yadutsa kutali ndi mitsinje kwapakidwa penti mmitengo ndi mmiyala.
Mwachindunji, kumadzulo malire yathu ndi mtsinje wa Dwazi, kumpoto kumene tagundizana ndi buloko ya Mandwe malire ndi Chimasomaso pamene mbali zina tidapaka penti, ndipo mbali imene tagundizana ndi buloko ya Chifwerekete kumwera, malire ndi mtsinje wa Kampongozi, pamene mbali zina tidapakanso penti.

UMWINI WA NKHALANGO

Nkhalangoyi ndi ya Boma ndipo ife tikuthandizana nawo kusamalila ndi kugwiritsa bwino ntchito zinthu zopezeka mmenemo malingana ndi mgwirizano umene ulipo.

ANTHU WOGWIRITSA NTCHITO NKHALANGOYI

Ife anthu akwa Gulupu Nyanja ndife eni ake oyambirira kugwiritsa ntchito nkhalangoyi komanso ena amadera ena ndiwololedwa kubwera kudzera mwa akomiti ya Nyanja Buloko kudzatenga zimene akufuna onse ogwiritsa ntchito nkhalangoyi ayenera kutenga chilolezo kwa akomiti

NTCHITO ZA NKHALANGO

Ndondomekoyi yapangidwa kuti anthu tizitengako zinthu izi: Milimo,matabwa, nkhuni zimene zili zowuma, bowa, mankhwala, matondo, zipatso, udzu, uchi luzi. Ntchito yina ndiyoti yimathandiza kuteteza nthaka kuti isakokoloke makamaka mmalo otsetseleka ndi mphepete mwa mitsinje.

MAPU YA NKHALANGO



Area (ha)	
Block	Area
Msankhile	740.6
Conservation area	411.2
Mpamila	434.7
Galum'tsuke	542.7
Chanika	707.5
Chenche	901.9
Kangolwa	631.6
Kasakula	871.7
Chifwelekete	445.9
Mnguluwe	250.1
Nyanga	179.7
Mkomba	496.5
Undi	520.4
Mandwe	379.2
Mpanang'ombe	604.5
Kajaliza	182.3
Mndinda	395.1
Sambakusi	337.8
Nyanja	727.8
Total Area	**9761.41ha**

ZIGAWO ZA KASAMALIDWE KA NKHALANGO YATHU

Buloko yathu ili ndi zigawo zenizeni zitatu.

CHIGAWO CHOYAMBA: Ichi ndi chigawo chimene chili mphepete mwa mitsinje ndi malo wotsetseleka woti atetezedwe. Kukula kwa chigawochi ndi pafupifupi 215.84ha.

CHIGAWO CHACHIWILI: Ichi ndi chigawo chimene munadulidwa mitengo chifukwa chotola matondo ndipo muli nkhuni zambili zowuma. Kukula kwa chigawochi ndi pafupifupi 11ha.

CHIGAWO CHACHITATU: Awa ndi malo wotsalawo amene kuli mitengo yambili ya masaizi yosiyanasiyana ndipo kukula kwake ndi pafupifupi 500.96ha.

MAPU YA NKHALANGO KUSONYEZA ZIGAWO ZA KASAMALIDWE KAKE

NYANJA CO-MANAGEMENT BLOCK NTCHISI DISTRICT



CHOLINGA CHACHIKULU CHA NDONDOMEKO INO

Kusamalila, kuteteza ndikugwiritsa bwino ntchito zinthu zopezeka mmenemo pothandizikira panyumba ndi pochita malonda ndicholinga chotukula miyoyo yathu

ZOINGA ZING'ONOZING'ONO

- ❖ Kufuna kupezamo Milimo, matabwa, nkhuni zogwiritsa ntchito panyumba ndi pochita malonda.
- ❖ Kufuna kuteteza mitsinje kuti isawundirizike ndi malo wotsetsereka kuti nthaka isakokoloke
- ❖ Kufuna kupezamo bowa, mankhwala, zipatso, udzu, matondo ndi uchi wogwiritsa ntchito panyumba ndi pochita malonda.

Cholinga choyamba chikufotokoza za mu chigawo chachitatu. Cholinga chachiwiri chikufotokoza za mu chigawo choyamba pamene cholinga chachitatu chikufotokoza za mzigawo zonse.

MALAMULO YA KAGWILITSIDWE NTCHITO KA ZINTHU ZA MNKHALANGO

Malamulowa ndi wokhudzana ndi Buloko yonse.

NO	LAMULO	CHILANGO
1	Osalowa mnkhalango (Buloko) opanda chilolezo	Wolakwira apereke nkhuku ziwiri
2	Osapha nyama komanso mbewa mnkhalango (Buloko) popanda chilolezo	Wolakwira apereke MK1,200.00
3	Osamweta udzu nkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeke atamweta udzu popanda chilolezo apereke MK200.00
4	Osatola nkhuni mnkhalango opanda chilolezo	Ngati munthu apezeke atatola nkhuni mnkhalango popanda chilolezo ayenera apereke MK50.00
5	Osacheka matabwa popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka atacheka matabwa azipereka MK5,000.00
6	Osatentha nkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka atatentha tchire popanda chilolezo azipereka MK10,000.00
7	Osakumba mtera mnkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka akukumba mtera mnkhalango popanda chilolezo ayenera apereke MK500.00
8	Osatenga dothi mnkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka atatenga dothi mnkhalango popanda chilolezo ayenera apereke MK200.00
9	Osadyetsa ziweto mnkhalango popanda chilolezo	Wodyetsa ziweto popanda chilolezo ayenera kupereka MK2,000.00
10	Osalima mnkhalango	Olima mnkhalango akapezeka alipire MK10,000.00

11	Osatcha mawaya nkhalango	Ngati munthu apezeka atatcha mawaya mnkhalango ayenera kupereka nkhuku zisanu ndi zitatu
12	Osaika ming'oma kapena kuweta njuchi mnkhalango popanda chilolezo	Wophwanya lamuloli ayenera kupereka nkhuku zisanu
13	Munthu saloledwa kumanga nyumba kapena khola mnkhalango popanda chilolezo	Wophwanya lamuloli adzalipira K5,000.00
14	Munthu saloledwa kuchotsa kapena kusintha malire a Buloko popanda chilolezo	Wophwanya lamuloli adzalipira nkhuku ziwiri kapena ndalama zokwana K700.00
15	Munthu aliyense ayenera kutenga nawo mbali pantchito zonse zosamalira Buloko.	Wosatenga nawo mbali adzalipira nkhuku imodzi kapena ndalama zokwana K350.00

DONGOSOLO LA KASAMALIDWE NDI KAGWILITSIDWE NTCHITO KA ZINTHU ZA MNKHALANGO
CHIGAWO CHACHITATU (FMU 3)

Chotengedwa mnkhalango: **Milimo** (Chenicheni)
Nkhuni – Zotsalira ku milimo
Matabwa – Azichekedwa pamene apezeka.

Mitundu yamitengo : Msolo, Msuku, Mpoka, Chiyere, Kasokolowe, Mkalakati, Nthengere
Yocheka matabwa – Nakaledza, Mpasa, Mbanga, Chimasomaso, Msenza, Mbawa, msenjere, mng'ona katope kasokolowe, chiyere, mtondo

Kufunidwa kwake : Kwambiri
Kupezeka kwake : Kwambiri zedi
Mabvuto :

- Milimo yambiri ikupezeka malo otsetseleka
- Anthu amatenga milimo opanda chilolezo
- Moto olusa umaotcha mitengo ya milimo
- Anthu kudula mosasamala

Njira zosamalila :

- Kudula mosamala osatsakamilitsa mitengo
- Odula milimo akhale ndi chilolezo komanso atsongozedwe ndi akomiti
- Kutenthera moyambirira
- Milimo idzadulidwa pamene mpata wapezeka nthawi zonse kuyambira Julaye 2008 kupita mtsongolo.
- Kudula mosankha

- Milimo idzadulidwa mugawo lachitatu la Buloko la Nyanja mmene muli mitengo yothinana.
- Milimo idzadulidwa malo osadutsa 33.3hekita pachaka mmakupu 16 a 2 hekitala imodzi ndipo adzakhazikitsidwa chaka chili chonse, mitengo 80 idzisiyidwa mukupu ili yonse osagwetsedwa. (Mpata woti mitengo ya milimo ifike poti yakula ndi zaka 15 mu Bulokoyi popeza muli mitundu ya mitengo yambili yosiyanasiyana.)
- Nkhuni zidzatoledwa zimene zinagwetsedwa nthawi yamatondo, zodzigwera zokha, zotsala kumilimo ndi kumatabwa.
- Matabwa – Munthu akhale ndi chilolezo chochekera matabwa ndipo atsongozedwe ndi akomiti, komanso adule mitengo yokhwima mosankha.
- Matabwa adzachekedwa pamene apezeka mmakupu okhazikitsidwa pachaka.

Kukula kwa malo : 33.3 hekitala. Milimo ndi nkhuni zidzatengedwa mmakupu okhazikitsidwa 16 pachaka.

Pa chaka: Akomiti zikakhale zogwiritsira ntchito panyumba zikakhala zogulitsa akomiti apereke chilolezo ndipo mkulu wazankhalango asainire

Wolandila chilolezo: Anthu ozungulira grulupu Nyanja ndi ena akwina.

Mtengo wa chiphaso chotolela milimo:

- Akuno K10.00 umodzi
- Akwina K50.00 umodzi.

Nkhuni:

- Akuno K10.00 pa mtolo umodzi
- Akwina K50.00 pamtolo ndipo pangolo K500.00.

Kucheka matabwa:

- Munthu ayenera alipire K7, 000.00 pamtengo umodzi.

CHOTENGEDWA KUNKHALANGO: ZIPATSO
CHIGAWO CHACHITATU (FMU 3)

Mitundu yamitengo yazipatso: Msuku, Mngokhomwala, Thenjere, Madazi, Nthudza, Kasokolowe,

Kufunika kwake: Kwambiri

Kupezeka kwake: Kwambiri

Mabvuto ake:
(a) Khwere zimadya zipatso zaziwisi.
(b) Moto wolusa umaononga maluwa azipatso
(c) Kudula mitengo yazipatso mwachisawawa.

Kasamalidwe kake:
(a) Osagwetsa mtengo potola zipatso.
(b) Kutenthera nkhalango panthawi yake.
(c) Kupukusa potola zipatso.
(d) Kutenga chotengera pokatola zipatso.
(e) Aliyense okatola zipatso atenge chilolezo Kwa akomiti.
(f) Zipatso zidzatoledwa mzingawo zonse za boloko kuyambira Okotobala mpaka Epulo

Kuchuluka Kwa zipatso zotoledwa pachaka:
Munthu akatenga chilolezo atole malinga ndi mene Zapezekela.

Wopereka chilolezo: Akomiti

Wolandira Chilolezo: Aliyense.

Mtengo wachilolezo: Aliyense ulere

CHOTENGEDWA KUNKHALANGO: MTERA
CHIGAWO CHACHITATU (FMU 3)

Mitundu ya mitengo ya mankhwala:
Mkalakati, m'bwazi, msolo, Maso ang'ombe, Mtengowaphira, madazi, thombodzi

Kufunika kwake: kwambiri.

Kupezeka kwake: kwambiri

Mavuto ake:

- moto wolusa umawononga zitsamba zonse
- Kukumba mankhwala mosasamala monga kugwetsa Mitengo
- Kusema mankhwala mtengo wonse
- Kupulula masamba ambiri kumtengo umodzi

Kusamala kwake:

- kutentha moto munthawi yake udzu usanaumitsitse
- Masamba asapululidwe ambiri kumtengo umodzi
- Osagwetsa mtengo wonse pofuna mankhwala
- Kukumba mankhwala mbali imodzi yamtengo
- Mankhwala adzatengedwa mzigawo zonse za BULOKO kuyambira Julaye mpaka mtsogolo

Kuchuluka kwa mtera otengedwa pachaka:
Mmene wapezekera

Wopereka chilolezo: Akomiti

Wolandira chilolezo: Munthu aliyense wofuna kupeza mankhwala

Mtengo wachilolezo:

- Anthu amu VDC ulele
- Akwina adzalipira K100.00 ngati chipondamthengo

CHOTENGEDWA KUNKHALANGO: MATONDO
CHIGAWO CHACHIWIRI (FMU 2)

Mitundu ya matondo: Matondo mtondo, matondo chitsulo, Matondo mvukwe

Kufunidwa kwake: Kwambiri

Kupezeka kwake: Kwambiri.

Mavuto:

- Kugwetsa mitengo yambiri potola matondo.
- Kuwotcha moto mosasamala

Kasamalidwe kake:

- Kutenthera panthawi yake.
- Kutola matondo okhwima amene agwa wokha
- Kuyendera mnkhalango kawirikawiri.

Kuchuluka Kwa matondo wotoledwa pachaka: Mmene angapezekere muzigawo zonse za buloko

Opereka chilolezo: Akomiti

Olandira chilolezo: Aeni wake wakwankuno komanso akumadera akutali.

Chilolezo chili motere:

- Akuno adzatenga mwaurere
- Akwina adzalipira ndalama yokwana MK100.00 ngati cholowera osawerengera kuchuluka kwa matondo otoledwa

Chotengedwa kunkhalango: Bowa

Chigawo chachitatu (FMU 3)

Mitundu yake: Chisuku, ndelema, chiwere, chipindi, manyame, Mkodzowagalu kasaza, mphofa, manda.

Kufunidwa kwake: Kwambiri.

Kupezeka kwake: Kwambiri.

Mavuto:

- Kugwetsa mitengo mwachisawawa imene imapangitsa kuti bowa umere.
- Moto wolusa umaotcha njere za bowa.

Njira zosamalira:

- Aliyense wokazula bowa azitenga chilolezo kwa akomiti
- Wokazula bowa azitenga potengera asavunge mmasamba
- Wosagwetsa mitengo imene imakonda bowa mwachisawawa
- Bowa uzizulidwa kuyambira mwezi wa Disembala mpaka Epulo chaka chilichonse ndipo uzizulidwa muzigawo zonse mmene ukupezeka.

Kuchuluka Kwa bowa wotengedwa pa chaka:

Munthu akatenga chilolezo azikazula malingana mmene wapezekera.

Wopereka chilolezo: Akomiti

Otenga chilolezo: Anthu wozungulira ndi ena akwina

Mtengo wa chiphaso chozulira bowa:

- Akuno azitenga mwa ulele.
- Akwina azilipira ndalama zokwana K50.00 ngati yolowera.

LUZI
Chigawo chachitatu (FMU 3)

Mitundu:	Mombo,kamphoni,msenga,
Kufunika kwake:	Kwambiri
Kupezeka:	Kwambiri
Mavuto:	Kukolola mosasamala Moto wolusa umaononga mitengo ya luzi.
Njira zosamalira:	Kumenya luzi la mmwamba ndi kuzotsalira za ku milimo Kutenthera kusanaumitsitse

Kukula kwa malo kapena kuchuluka kwa luzi pa chaka:
Momwe lapezekera

Opereka chilolezo:	Akomiti
Otenga chilolezo :	Aliyense
Mtengo wa chilolezo:	Akonkuno azilipira ndalama zokwana K100.00 ngati yolowera K200.00 kwa anthu onse ochokera kwina ngati yolowera

UCHI CHIGAWO CHACHITATU (FMU 3)

Mitundu:	Uchi wa Msanga.
Kufunika kwake:	Kwambiri
Kupezeka:	Pang'ono

Mavuto:

- Kuchepa kwa njuchi.
- Kukolola moyipa
- Moto umaononga mitengo ndi njuchi.

Njira zosamalira:

- Pofula osatenga moto woyaka.
- Wofuna kuweta njuchi ayike ming'oma ya makono ndipo akhale ndi chilolezo kuchokera kwa akomiti
- Ming'oma idzapachikidwa mu gawo la chitatu la buloko ndipo nthawi iliyonse kuyambira Julaye mpaka mtsogolo.

Kukula kwa malo kapena kuchuluka kwa ming'oma yopachikidwa pa chaka:
Amene watenga chilolezo apachike ming'oma mmene Angathele

Opereka chilolezo: Akomiti

Otenga chilolezo: Wozungulira Nyanja Buloko

Mtengo: K50.00 pa mng'oma pa chaka.

NDONDOMEKO YAKAGWILIDWE KA NTCHITO YOSAMALILA BULOKO YA NYANJA

NO.	NTCHITO	ZIPANGIZO	KALOZERA	WOCHITA	NTHAWI
1	Kukonza malire wokhazikika	Penti Bulashi Zikwanje Silasha	Malire wokhazikika wopakidwa ndi penti.	Mafumu, Akomiti Alangizi	Sabata yoyamba ya mwezi wa Julaye
2	Kuyendera	Zikwanje Silasha	Malipoti	Akomiti Alangizi Mafumu Anthu amudzi	Sabata yoyamba ya Julaye mpaka mtsongolo
3	Kutenthera	Moto Zikwanje Silasha Keni Madzi	Malo opaza moto ndi ziphukira	Akomiti Alangizi Mafumu Anthu amudzi	Julaye
4	Kuchita misonkhano yazankhalango	Zolembera Makope	Malipoti/malekodi	Akomiti Alangizi Mafumu Anthu amudzi	Kuyambira Julaye mpakana May chaka china
5	Kupereka zilolezo	Zolembera Malisiti Mabuku	Malekodi	Akomiti Alangizi	Kuyambira Julaye mpakana Juni chaka china
6	Kulemba malipoti ndu kupereka koyenerera monga kuofesi, Bungwe loyang'ana nkhalango yonse	Mapepala Zolembera	Lipoti	Akomiti Mafumu	Mwezi ndi mwezi
7	Kutola matondo	Ndowa Nthumba	Nambala yandowa ndi matumba otengedwa	Akomiti Mafumu Anthu amudzi	November mpaka Decembala
8	Kutola nkhuni	Luzi Nkhwangwa Zikwanje	Nambala yamitolo yotoledwa	- Akomiti - Alangizi	Kuyambira Julaye mpaka Junichaka china
9	Kutola zipatso	Ndowa Thumba	Nambala yandowa ndi matumba yotoledwa zipatso	- Akomiti - Mafumu - Anthu amudzi	Kuyambira Julaye mpaka Juni chaka china
10	Kuzula bowa	Ndowa Thumba Dengu	Nambala ya ndowa ndi matumba	- Akomiti - Mafumu - Anthu amudzi	Kuyambira Novembala mpaka April

			wozulidwa ndi bowa		
11	Kumweta udzu	Chisikiro Chikwanje Khasu	Nambala yamitolo yaudzu	- Akomiti - Mafumu - Anthu amudzi	Kuyambira Julaye mpaka Okutobala
12	Kukumba makhwala	Makasu Zikwanje Thumba	Nambala yazikunje zamankhwala otengedwa	- Akomiti - Mafumu - Anthu amudzi	Kuyambira Julaye mpaka Juni chaka china
13	Kufula uchi waming'oma	Ndowa Mvukuto Zobvala zofulira uchi	Nambala yandowa zofulidwa zauchi	- Akomiti - Mafumu - Anthu amudzi - Alangizi	Kuyambira Julaye mpaka Juni
14	Kuunika malamulo	Zolembera Makope Mapepala Chakudya	Maliupoti Malekodi	- Akomiti - Mafumu - Anthu amudzi - Alangizi	Kumapeto kwa Juni kulikonse
15	Kukonza tizigawo tokololamo milimo(Makupu)	Zikwanje Nkhwangwa Penti Palaffini Bulashi Magolovesi	Nambala ya tizigawo tokhazikika topakidwa penti	- Akomiti - Mafumu - Anthu amudzi - Alangizi	Julaye

NDONDOMEKO YOYENDELA KUNKHALANGO

MALO	OCHITA	ZIPANGIZO	NTHAWI
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a zamnyunda ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yoyamba ya julaye
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu aNyanja I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachiwiri ya julaye
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu aNyanja II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachitatu ya julaye
Malo amitengo yothinana	Amfumu a Nkhalawangwe ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachinayi ya julaye
Mbali mwa mitsinje	Amfumu a Zambala II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera Mabuku	Sabata yoyamba ya Ogasiti
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu aNgoma ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zolembera Zikwanje Mabuku	Sabata yachiwiri ya Ogasiti
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Zambala I ndi anthu awo - Alangizi - Akomiti	Mabuku Zolembera Zikwanje	Sabata yachitatu ya Ogasiti
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Kankowe II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Mabuku Zolembera	Sabata yachinayi ya Ogasiti
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu akankowe I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yoyamba ya Seputembala

Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Nyanja I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachiwiri ya Septembala
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Zamnyunda ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera Mabuku	Sabata yachitatu ya Septembala
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Nyanja I I ndi anthu awo - Alangizi - Akomiti	Mabuku Zolembera Zikwanje	Sabata yachinayi ya Septembala
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu aNyanja II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachitatu ya julaye
Malo amitengo yothinana	Amfumu a Nkhalawangwe ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachinayi ya julaye
Mbali mwa mitsinje	Amfumu a Zambala II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera Mabuku	Sabata yoyamba ya Ogasiti
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu aNgoma ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zolembera Zikwanje Mabuku	Sabata yachiwiri ya Ogasiti
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Zambala I ndi anthu awo - Alangizi - Akomiti	Mabuku Zolembera Zikwanje	Sabata yachitatu ya Ogasiti
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Kankowe II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Mabuku Zolembera	Sabata yachinayi ya Ogasiti
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu akankowe I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yoyamba ya Septembala
Malo amitengo	- Amfumu a Nyanja	Zikwanje	Sabata yachiwiri ya

yothinana	I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zolembera mabuku	Seputembala
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Zamnyunda ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera Mabuku	Sabata yachitatu ya Seputembala
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Nyanja I I ndi anthu awo - Alangizi - Akomiti	Mabuku Zolembera Zikwanje	Sabata yachinayi ya Seputembala
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu aNkhalawangwe ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yoyamba ya Okotobala
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Zambala II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachiwiri ya Okotobala
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Ngoma ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera Mabuku	Sabata yachitatu ya Okotobala
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu aZambala I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zolembera Zikwanje Mabuku	Sabata yachinayi ya Okotobala
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Zamnyunda ndi anthu awo - Alangizi - Akomiti	Mabuku Zolembera Zikwanje	Sabata yoyamba ya Novembala
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Zambala II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Mabuku Zolembera	Sabata yachiwiri ya Novembala
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu a Nyanja I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachitatu ya Novembala
Malo amitengo	- Amfumu a Ngoma	Zikwanje	Sabata yachinayi ya

yothinana	ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zolembera mabuku	Novembala
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Kankowe II ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera Mabuku	Sabata yoyamba ya Disembala
Malo amitengo yothinana	- Amfumu a Kankowe I ndi anthu awo - Alangizi - Akomiti	Mabuku Zolembera Zikwanje	Sabata yachiwiri ya Disembala
Malo otsetsereke ndi malo ogwetsedwa ndi matondo	- Amfumu a Zamnyunda ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachitatu ya Disembala
Mbali mwa mitsinje	- Amfumu a Zambala I ndi anthu awo - Akomiti - Alangizi	Zikwanje Zolembera mabuku	Sabata yachinayi ya Disembala

DONGOSOLO LOCHITILA KALONDOLONDO

CHOLINGA	ZOMWE TINGADZAYESE	KAYESEDWE	KALOZERA	OCHITA	ZIPANGIZO	NTHAWI
Kuteteza mmitsinje ndi malo otsetseleka	- Kupezeka kwa mitengo m'mbali mwa msinje. - Kukhala ndi madzi osaphwa	Kuwona	Kupezeka kwa madzi	-Akomiti - Alangizi - Anthu Amfumu	- Zikwanje - Silasha	Chaka chili chonse
Kufuna kupezamo bowa, mankhwala, zipatso, udzu, matondo, ndi uchi wogwiritsa ntchito panyumba ndipochita malonda	Kupezaka kwa bowa, mankhwala, zipatso, udzu, matondo ndi uchi	Kuwona	Nambala yamatumba otengedwa	-Akomiti - Alangizi - Anthu Amfumu	- Zikwanje - Silasha	Chaka chili chonse kuyambira Julaye
Kufuna kupezamo milimo,matabwa ,nkhuni zogwiritsa ntchito panyumba ndi pochita malonda	Kupezeka kwa nkhuni	Kuwona	Kuchuluka kwa ndalama zopezeka pogulitsa milimo Matabwa, nkhuni.	-Akomiti - Alangizi - Anthu Amfumu	- Zikwanje - Silasha - Nkhwangwa	Chaka chili chonse kuyambira Julaye

DONGOSOLO LA ZACHUMA

Ndalama zonse zopelekedwa ku komiti zidzagwiritsidwa ntchito malinga ndi malamulo oyendetsera gulu lathu.

MALAMULO YA NYANJA BULOKO
CHOLINGA CHAGULU
Kuteteza ndi kugwiritsa bwino ntchito zithu zopezeka mu Nyanja Buloko.

MNDANDANDA WAGULU

- Muzikhala a maudindo monga; wapampando ndi wachiri wake, mlembi ndi wachiwiri wake, msungi komanso amphika nkhani asanu (5). Onsewa ayenera akhale oyimirira magulu ogwiritsa ntchito zithu zosiyanasiyana zamnkhalango.

- Muzikhala mafumu, agulupu ndi anthu ozugulira midzi ya Kankowe I ndi II, Zamnyunda, Zambala I ndi II, Ngoma, Nyanja I ndi II, Nkhalawangwe.

WAPAMPANDO NDI WACHIWIRI WAKE
ZOMUYENEREZA

- Akhale nzika yamidzi ya Kankowe I ndi II, Zamnyunda, Zambala I ndi II, Ngoma, Nyanja I ndi II, Nkhalawangwe.

- Akhale wolimbikira ntchito zankhalango.
- Akhale munthu wambiri yabwino.
- Akhale munthu wopanda tsankhu.

NTCHITO ZAWO

- Kukonza msonkhano
- Kutsongolera kuti titeteze chilengedwe
- Kulimbikitsa gulu kuti lisafooke
- Kulandira msonkhano

MLEMBI NDI WACHIWIRI WAKE ZOMUYENEREZA

- Akhale wodziwa kulemba ndi kuwerenga
- Akhale wachangu pochita zithu
- Akhale wosaiwalaiwala akauzidwa zithu
- Akhale nzika ya midzi ya Kankowe I ndi II, Zamnyunda, Zambala I ndi II, Ngoma, Nyanja I ndi II, Nkhalawangwe.

NTCHITO ZAWO

- Kulemba makalata yodziwitsa anthu zamsonkhano
- Kulemba katundu wagulu
- Kulemba za pamsonkhano komanso kuwerenga zamsonkhano wopita
- Kulemba malipoti yakagwiridwe kantchito ndi kufotokozera gulu.

MSUNGI ZOMUYENEREZA

- Akhale wosachokachoka
- Akhale wosaononga katundu
- Akhale wodziwa kuwerenga katundu wolowa ndi wotuluka
- Akhale nzika yamidzi isanu ndi inayi imeneyi

NTCHITO ZAKE

- Kusunga katundu wagulu amene alipo
- Kulembera katundu wolowa ndi wotuluka
- Azipereka lipoti lakatundu kugulu

KOMITI MEMBALAZOWAYENEREZA

- Akhale nzika yamidzi ya kamkowe I ndi II, Zamnyunda, Zambala I ndi II, Ngoma, Nyanja I ndi II, Nkhalawangwe.
- Akhale wachangu akaitanidwa kumsonkhano

NTCHITO ZAKE

- Kuphika nkhani zamkomiti
- Kukumbutsa wapampando ngati komiti sikuyenda bwino
- Kuona ntchito zamgulu ngati zikuyenda kapena ayi.
- Kutumikira mukomiti

NTHAWI YOKHALIRA PAUDUNDO

Anthu onse ammudzi anagwirizana kuti mu Buloko ya Nyanja munthu azikhala pa udindo kwa zaka zitatu basi. Zikatha zaka zitatu a gulupu aziitana msonkhano wosankha anthu ena kuti akhale mmaudindowo.

ZOMUCHOTSERA MUNTHU PAUDUNDO

- Waulesi
- Wosaweruzika

MPHAMVU ZA AKOMITI

- Azikumana ndi kukambirana za ntchito komanso kukonza ndodomeko ya ntchito
- Kuonetsetsa kuti Buloko ya Nyanja ikusamalika.

KATHETSEDWE KAKOMITI

- Ngati ikuchita ulesi
- Pakatha zaka zitatu

UMEMBALA WAGULU

- Munthu aliyense wamidzi ya kamkowe I ndi II, Zamnyunda, Zambala I ndi II, Ngoma, Nyanja I ndi II, Nkhalawangwe ali ndi ufulu wokhala membala wa gulu.
- Agulupu aziitana anthu onse amidzi isanu ndi inayi pakatha zaka zitatu ndi kuchititsa masankho
- Kasakhidwe kake kazikhala kochita voti munthu modzi kuvota kamodzi paudindo.
- Agulupu adzachititsanso masankho mwadzidzidzi ngati komiti yathestsedwa kamba ka zifukwa zina.

ZOMUCHOTSETSA MUNTHU MUGULU

- Ngati sakulimbikira ntchito zankhalango
- Ngati wapezeka ndi milandu ndipo wakanika kuweruzidwa.

UFULU WOCHITA APILO PAMILANDU

- Munthu akachotsedwa mgulu ali ndi ufulu wokagwada kwa amfumu wake, akalephera uko apite kwa agulupu kapena kwa T/A kenake kukhoti.
- Ndipo kumeneko ngati akhutira ndi dadaulo lake akhoza kumubwezeretsa mgulumo popanda chovuta, ngati sanakhutire basi ndiye kuti munthuyo/anthuwo achotsedwa basi.

NTCHITO ZAGULU LONSE

- Kusamalira zithu zopezeka muBulokoya Nyanja
- Kuona komiti ngati ikukwaniritsa ntchito zake
- Kuyang'anira wina ndi mzake kuti tisaononge Nyanja Buloko.
- Kusankha anthu kuti akhale mmaudundo
- Kukonza/kuunika malamulo yoyendetsera gulu.

MISONKHANO

- Komiti izikumana kawirir pamwezi kukambirana zantchito ndipo anthu ayenera kuti afike theka kuti zokambirana ziyambike.
- Msonkhano wakomiti ndi gulu lonse uzichitika kamodzi pamwezi kukambirana zantchito. Anthu ayenera kuti afike, theka akomiti, kuphatikizanso theka mamembala ena.

MALAMULO OYENDTSEARA GULU

NO	LAMULO	CHILANGO
1	Osalowa mnkhalango (Buloko) opanda chilolezo	Wolakwira apereke nkhuku ziwiri
2	Osapha nyama komanso mbewa mnkhalango (Buloko) popanda chilolezo	Wolakwira apereke MK1,200.00
3	Osamweta udzu nkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeke atamweta udzu popanda chilolezo apereke MK200.00
4	Osatola nkhuni mnkhalango opanda chilolezo	Ngati munthu apezeke atatola nkhuni mnkhalango popanda chilolezo ayenera apereke MK50.00
5	Osacheka matabwa popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka atacheka matabwa azipereka MK5,000.00
6	Osatentha nkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka atatentha tchire popanda chilolezo azipereka MK10,000.00
7	Osadula mtengo potola matondo	Wodula mitengo ayenera kupereka MK5,000.00
8	Osakumba mtera mnkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka akukumba mtera mnkhalango popanda chilolezo ayenera apereke MK500.00
9	Osatenga dothi mnkhalango popanda chilolezo	Ngati munthu apezeka atatenga dothi mnkhalango popanda chilolezo ayenera apereke MK200.00
10	Osasema mtengo mozugulira pofuna mtera, kapena kudula mizu yonse mozugulira mtengo	Ngati munthu asema/kudula mizu mtengo mozugulira pofuna mtera ayenera kupereka mbuzi imodzi kapena MK2,000.00
11	Osadyetsa ziweto mnkhalango popanda chilolezo	Wodyetsa ziweto popanda chilolezo ayenera kupereka MK2,000.00
12	Osalima mnkhalango	Olima mnkhalango akapezeka alipire MK10,000.00
13	Osatcha mawaya nkhalango	Ngati munthu apezeka atatcha mawaya mnkhalango ayenera kupereka nkhuku zisanu ndi zitatu
14	Amene watenga chilolezo chotolera zipatso atole zakupsya kapena zogwa zokha asachite kupulula masamba kapena kudula mtengo	Wopezeka atadula mtengo kapena kupulula masamba amtengo potola zipatso ayenera kupereka MK5,000.00
15	Osaika ming'oma kapena kuweta njuchi mnkhalango popanda chilolezo	Wophwanya lamuloli ayenera kupereka nkhuku zisanu

KAYENDETSEDWA KA ZACHUMA

- Amsungi ndi amene azisunga ndalama zonse
- Ndalama zizikasungidwa ku Banki imene itsekulidwe ndipo osainira wake ndi wapampando, mlembi ndi msungi.

KAPEREKEDWE KA MADIPO

- Munthu amene wapezeka ndi milandu sazigwira nawo ntchito mugulu kufikira atalipira milanduyo.
- Zolipira zonse ziziperekedwa kwa msungi ndipo chikakhala chiweto chizigulitsidwa ndipo iye azisunga ndalama

KASUNGIDWE KAMALEKODI

Gulu linagwirizana kuti lizisunga malekodi ake motere:-

1. Buku landalama losonyeza zolowa ndi zotuluka (azisunga ndi msungi)
2. Buku luBanki
   - Ili litsekulidwa ndipo ndimmene ndalama zonse ziziikidwa
   - Wapampando, mlembi ndi msungi ndi amene azisainira pofuna kugwiritsa ntchito ndalamazo (Wosunga bukhuli ndi msungi)
3. Buku lamayina ya mamembala
   - Ili lizikhala bukhu la kaundula wamamembala lomanso losonyeza amene wagwira ntchito ndi tsiku lake, kapenanso amene wapezeka pamsonkhano (wosunga ndi mlembi)
4. Buku la katundu
   - Muzilembedwa katundu wagulu yemwe walandiridwa/wagulidwa ndi yemwe watuluka.
5. Buku lolembamo zamisonkhano
   - Umumuzilembedwa zonse zomwe gulu lakambirana.
6. Buku lamilandu
   - Umu muzilembedwanso munthu amene wapalamula, zomwe walipira ndi tsiku lilipirira.
7. Buku la chilolezo
   - Umu muzilembedwa chilolezo chomwe chaperekedwa ndi ntchito yake, munthu amene walandira ndala zomwe walipira, tsiku lothe chilolezo ndi wokamuyang'anira pogwira ntchito yachilolezo.
8. Buku la matikiti.
   - Pazikhala mtengo wolipira katundu magulu
9. Buku la alendo
   - Alendo onse azisaina mbukuli, ntchito yomwe adzagwira, (Adilesi) keyala ndi tsiku.
10. Buku la anthu/magulu ochita mabizinesi azithu zochokera mnkhalango

- Umu muzikhala dzina la munthu/gulu, bizinesi imene akuchita, tsiku lolembetsera.

KAYENDETSEDWE KA ZANGONGOLE

- Ndalama zagulu zitha kubwerekedwa kwa munthu/gulu lofuna kuchita bizinesi koma akhale a mu Nyanja Buloko komanso akahale a makhalidwe a bwino.

- Chiongola dzanja ndi 25% ndipo munthu ayenera kuyamba kukongola K1,000.00 koma ayenera kubweza pakatha mwezi umodzi.

- Munthu/gulu likakanika kubweza ndalamazo komiti iyenera ipite nayo nkhani kwa amfumu akakanika kwa amfumu wake nkhani ipite kwa gulupu kenako kukhoti.

KUSASIYANA MUGULU PACHILICHONSE

- Padzakhala kufanana pochita zithu pakati pa amai ndi abambo kuyambira pogwira ntchito. Kasankhidwe kamaudindo komanso kagawanidwe kaphindu.

- Sipadzakhala kukondera mbali pochita zithu

KUWUNIKA MALAMULO

- Malamulo aziwunikidwa chaka chili chonse.

- Agulupu aziyitanitsa msonkhano wagulu lonse kuti malamulo awunikidwe kumapeto kwa chaka chiri chonse.

KAGAWANIDWE KAPHINDU LOPEZEKA MUNYANJA BULOKO

Phindu lopezeka munkhalango ndi ili:-

(a). Bowa
(b) Nkhuni
© Ngumbi
(d) Matabwa
(e) Luzi
(f) Nyama
(g) Milimo
(h) Mipini
(i) Uchi
(j) Mankhwala
(k) Zipatso
(l) Chinaka

1. **BOWA, NGUMBI, ZIPATSO, CHINAKA, UDZU:-**

- Banja lililonse lizikatenga chilolezo chokatengera zithu zimenezi mwaulere ngati ndi zokagwiritsa ntchito panyumba.

2. **NKHUNI, MITENGO YAMATABWA, LUZI, NYAMA, MILIMO, MIPINI, UCHI, MANKHWALA NDI ZINA.**

- Banja lirilonse lizikatenga chilolezo kwa wapampando ndipo lizikalipira monga mtengo wake malingana ndi (Licensing Plan) ndondomeko

- Ndalama zake zizikasungidwa kuBanki ya Nyanja Buloko

- Ndalamazo ntchito zake ndi izi:-
  - Kugwira ntchito za chitukuko cha mmudzi (i.e monga kuthandizika pamaliro etc)
  - Kuthandiza posamalira Nyanja Buloko
  - Kuthandiza magulu yamabizinesi yamuNyanja Buloko powabwereketsa
  - Kuthandiza akomiti kuti athe kuyendetsa bwino gulu (i.e monga kugulira mabuku yosiyanasiyana, kuthandiza pamisonkhano)
  - Kuthandiza kuti gulu lithe kupeza luso (maphunziro) ya zankhalango.

KUYAMBA KUGWIRA NTCHITO KWAMALAMULO.

- Malamulo ya Nyanja (Buloko) adzayamba kugwira ntchito pa 1st Julaye, 2008

WOSAINILA

Mkhalapampando **Tsiku……..**

Group Village headman **Tsiku ……..**

Gogochalo **Tsiku ……**

Mkulu wa zankhalango **Tsiku …….**